



*M'busa Alamo ndi malemu mkazi wake Susan pa pulogalamu yawo ya pakanema wa dziko lonse amene anajambulidwa ku Grand Ole Opry, Nashville, Tennessee chithunzi—1975*

adzakopa anthu onse m'dzikoli]: Amene mafumu a dziko anachita naye chigololo [Mwafanizo, izi zikutanthauza iwo amene atengera mabodza ake. Iwo achita chili-chonse chonyansa (tchimo lonyasa) padziko lapansi, ndipo iwo ndi amene amachititsa nkhondo zonse komanso kupha anthu, kuphatikizapo kupha kwa KHRISTU, aneneri, ndi woyerwa mitima.]” (Chivumbulutso 17:1-2).

M'masomphenya, mneneri Danieli anaona chirombo choopsa ichi. Anaona chirombo ichi, boma la dzikoli, monga “choopsa ndi chochititsa mantha, ndi champhamvu kwambiri; ndipo chinali nao mano akulu achitsulo: chinalusa ndi kuphwanya kukhala m'zidutswa, ndikuponda chot-



# Babulo wa Chinsinsithe Make wa Achigololo

**Yolembendwa ndi Tony Alamo**

Mtumwi Yohane anati, “Ndipo anadza m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri amene anali ndi mbale zolowa zisanu ndi ziwiri [za mkwiyo wa MULUNGU, umene posachedwapa udzakhuthulidwa pa dziko lapansi<sup>1</sup>], ndipo analankhula ndi ine, nanena nane, Bwera kuno; Ndizakusonyeza iwe chiweruzo cha hule wamkulu amene akukhala pa madzi ambiri [mawu akuti “madzi ambiri” ndi ofanizira, kutanthauza mitundu yambiri; iye

sala ndi mapazi ake: ndipo chiniali chosiyana ndi zirombo zonse [maufumu] zimene zinali patsogollo pake; ndipo chinali ndi nyanga khumi” (Danieli 7:7). Palibe ngati boma ili ndipo sizinachitikepo ndi kale lonse padziko lonse.

Ena mwa anthu amu Babulo wa Chinsinsi (a Vatican, Tchalitchi cha Roma Katolika) amakondadi YEHOVA. Awa ndi wosadziwa a maudindo ang'onoang'ono. Komabe, ndondomeko ya maudindo ndiyauchimo ndi yoipa mosayerekezeka! Iwo amati choipa chimene anachita kale ndi chakale, koma mwanseli, mpaka lero, akhala akupha anthu ambiri kuposa kale lonse. Iwo amati savomereza kuchotsa mimba, kugonana amuna kapena akazi okhaokha, ndi zolau-

la, koma chifukwa iwo ndiboma la dziko, amalamulira boma la dziko, ndipo ndi iwo amene amayambitsa zoipa zonse padziko lapansi.<sup>2</sup> Ichi ndi chifukwa chake MULUNGU anauza Akhristu wamba osalakwa onse “TULUKANI M'MENEMO [hule], ANTHU ANGA, kuti inu musakhale oyanjana nawo machimo ake, ndi kuti musalandire miliyi yake [mkwiyo wa MULUNGU]” (Chivumbulutso 18:4).<sup>3</sup> “Ndipo iwo akukhala padziko lapansi [dziko lonse lapansi] analedzera ndi vinyo wa chigololo chake [machimo onse. Iye ndi wandale ndi wachipembedzo chonama]” (Chivumbulutso 17:2).

Chivumbulutso 17:9 akuti, “Ndipo apa pali mtima wakukhala (Yapitirira patsamba 2)

## BABULO WA CHINSINSI MAKE WA ACHIGOLOLO

(Yachokera patsamba 1)

nayo nzeru. Mitu isanu ndi iwi-ri ndiyo mapiri asanu ndi awiri, amene mkazi [Vatican, mneneri wonyenga, hule lalikulu] akhalapo.” Ngati mutumiza imelo kapena kuyimbira kampani yothandiza anthu apaulendo ndi kuwafunsa za tikitayopitira ku mzinda wa mapiri asanu ndi awiri, iwo akugulit-sani tikitayopita ku Rome, Italy!

Mtumwi Yohane anaonetsedwa “chodabwitsa china m’mwamba; ndipo taonani chinjoka chofifira chachikulu, chakukhala nayo mitu isanu ndi iwiri [mapiri asanu ndi awiri a Rome] ndi nyanga khumi, ndi pamutu pake nduwira zach-ifumu zisanu ndi ziwiri [kuchiika chinjokachi ngati chotsogolera usatana (chirombo) wa makontinenti a dziko]. Ndipo mchira wake uguza limodzi la magawo atatu a nyenyezi [chizindikiro cha angelo oipa osamvera. Chivumbulutso 1:20 amati nyenyezi ndi angelo] za Kumwamba, nuziponya padziko” (Chivumbulutso 12:3-4).<sup>4</sup>

Rome ndiwoitanidwa ndi MULUNGU, osati Babulo, koma “BABULO WA CHINSINSI WANKULU.”<sup>5</sup> Palibe mpingo wamwambo wabodza umene ukankhoza konse kuzindikiridwa bwinobwino ndi MAWU a MULUNGU ngati umenewu (Vatican) ukutchulidwa mu Chivumbulutso 17: 3-9: Choncho mngelo anamutenga Yohane “mu MZIMU [wa MULUNGU] kunka naye m’chipululu: ndipo ine [Yohane] ndinaona mkazi atakhala pachirombo chofiritsa [mneneri wachinyengo wachizimayi wa Roma ndiponso wandale zaupan-du atakhala pa mtundu wofiritsa wa gulu la upandu la makadinala, chirombo chofiritsa nkukhala

boma la dziko lonse lotsogole-redwa ndi Vatican], chodzala ndi maina a mwano, chakukhala nayo mitu isanu ndi iwiri [mapiri asanu ndi awiri a Rome] ndi nyanga khumi [mitundu khumi yaku Ulaya, imene kwa nthawi yochepa in-amujoina, kenako ndikumutentha (Chivumbulutso 17:16)].

“[Ndipo pano pali mitundu ya miyambo ya upandu.] Ndipo mkazi anabvala za mtundu wa pepo ndi wofifira, zokometsedwa ndi golidi ndi miyala ya mtengo wake ndi ngale [pamene omutsatira ake akukhala muumphawi ndi uve osaneneka], nakhala na-cho m’dzanja lake chikho chagolidi chodzala ndi zonyansitsa [zimene zili machimo oipitsitsa], ndi zodetsa za chigololo chake: Ndipo pamphumi pake padalembedwa dzina, CHINSINSI, BABULO WANKULU, MAI WA ACHIGOLOLO NDI WA ZONYANSITSA ZA DZIKO LAPANSI.

“Ndipo ine [Yohane] ndinaona mkazi woledzera ndi mwazi wa oyera mtima, ndi mwazi wa mbo-ni za YESU: ndipo nditamuona, ndinazizwa ndi kusilira kwaku-kulu. [Chinyengo cha mdier-ekezi ndichakuya kwambiri kwa-kuti ngakhale Mtumwi Yohane anatengeledwa ku chisiliro cha masomphenya a upandu a mdier-ekezi, ndi chionetsero chake, mi-yambo, nyimbo, mikanjo yapam-wamba, golide, ngale, chuma, ndi zina zambiri] Ndipo mngelo anati kwa ine, Uzizwa chifukwa ninji? ine ndidzakuza iwe chinsinsi cha mkazi [mneneri wonyenga wamkazi], ndi cha chirombo chakumbereka iye [ndi boma la dziko limene limamvera malamulo ake. Mphamu zake ndizochokera kwa chirombo chachikulu chofifira, mdierekezi (Chivumbulutso 13:4)], chokhala nayo mitu isanu ndi iwiri [mapiri asanu ndi awiri a

Rome] ndi nyanga khumi [maiko khumi aku Ulaya].

“Chirombo [choutsidwa] chimene unachiona chinaliko [nthawi ina yake, Rome anali mfumu ya dziko], koma kulibe [Rome anagwa]; ndipo [kuukanso] chidzaturuka m’phompho, ndi kunka kuchitayiko [Rome, ndi mphamu ya mzimu wa Satana, mdier-ekezi, anaukanso kunka m’dziko nanamizira ngati mpingo, ndipo ndiwoposa kwambiri chilichonse chimene aliyense angaganizire kuti ndi cholakwa<sup>6</sup>]: Ndipo adzazizwa iwo akukhala padziko [Satana ndi nyenga wamkulu].<sup>7</sup> Ngakhale kwa mphindi imodzi, Mtumwi wamkulu Yohane anapusitsidwa ndi Satana. Zinyengo zonse zimathawa ukadziwa KHRISTU, AMENE ALI MAWU A MULUNGU, mu Baibulo la King James Version.<sup>8</sup> Amadabwa], amene maina awo sanalembewe mu Bukhu la Moyo chiyambire makhazikidwe a dziko lapansi, pakuona chirombo chimene chinaliko, ndipo kulibe, ndipo chidzakhalako.

“Ndipo [kachikenanso,] pano pali mtima wakukhala nayo nzeru. Mitu isanu ndi iwiri ndiyo mapiri asanu ndi awiri, amene mkazi akhalapo.” Chinjoka (Satana, mdierekezi) chinachipatsa ulamuliro umenewu chirombocho ndi mphamu zonyenga dziko lonse (Chivumbulutso 13:2,4). Zonsezi zikuchitika panapa! Lapani machimo anu. Yambani

(Yapitirira patsamba 4)

<sup>6</sup> Chiv. 13:3 7 Gen. 3:1-6, Mat. 24:11-12, 24, Yoh. 8:44, 2 Kor. 11:13-15, 2 Ates. 2:3-12, 2 Tim. 3:13, 1 Yoh. 4:1, 2 Yoh. 7, Chiv. 2:9, 12:9, 13:1-8, 11-15, 16:13-14, 17:8, 19:19-21, 20:1-3, 7-8 8 Masa. 119:105, Miy. 6:23, Yoh. 1:1-3, 10-14, 1 Yoh. 1:1-3, 5:7, 20, Chiv. 19:11-16



MAUTUMIKI A ALAMO PA INTANET  
[www.alamoministries.com](http://www.alamoministries.com)

## Africa Zambia

Ndikutengerapo mwayi kukuthokozani kwambiri chifukwa cha zimene mukutichitira ife omvera Radio East Africa. Kale, ndinene kuti sindinali woyenelera konse pamaso pa Mulungu. Koma kumvera wailesi yanu kwasinthiratu moyo wanga. Ine tsopano ndikugwira ntchito ngati mtumiki wabwino wa Mulungu.

Luka Chaiwira

Livingstone, Zambia

## Cameroon

(*Zomasulira kuchoka mu Chifaransa*)

Wokondedwa Abusa,

Ine ndikukudziwitsani za chimwemwe tili nacho pakati pathu, kwa abale athu a Chisilamu amene alandira Khristu monga Mpulumutsi wao ndi Mbuye wao kudzera mu zolemba zanu za Chikhristu, nkhani zam'makalata. Ilipo miyoyo makumi atatu kuchokera kumpoto kwa dzikolo. Ndikufuna maBaibulo ena a iwo. Wokondedwa Abusa, tikufuna mabuku a Mesiya, ndi makatoni awiri a zolemba zanu pa zopempha zathu.

Ella Engelbert

Republic of Cameroon

## Missouri

Okondedwa Utumiki wa Tony Alamo, Ndikulemba ndi cholinga cho-kuthokozani chifukwa cha mabuku amene munanditumizira. Ndiwothandiza kwambiri kwa ine. Ine ndine Mkhristu watsopano ndipo zinthu zimene amalemba M'busa Alamo m'nkhani zam'makalata za dzikolonse zinandilimbiktsa kwambiri. Ndakhala ndikupita ku tchal-itchi m'mbuyomu koma osandifikasi-po, koma tsopano ndikuchimva kuti ndafika poyenelera. Ndikadzatuluka ndikufunitsitsa kudzakhala m'modzi wa Tony Alamo Christian Ministries. Pitilizani kutumiza timabuku kuti ndikule m'chikhulupiriro changa cha Chikhristu ndi kukhala munthu amene Yesu akufuna ndikhale.

Daniel Wilson  
Farmington Correctional Center  
Farmington, MO

## Pakistan

Wokondedwa M'bale Tony Alamo mwa Khristu,

Moni m'dzina la Yesu. Ndikukuthokozani kwambiri chifukwa chotitumizira zolemba zanu za Uthenga Wabwino. Lero ndalandira katundu ndi zolemba zanu zonse zimene munatumiza.

Tsopano ndikukutumizirani zithunzi za katundu amene ndinalandira. Ndikufuna kukuthokozaniso chifukwa cha katunduyo. Mawa, ndiyamba kuga-wa zolemba zanuzi m'madera osiyanasiyana. Tikukhulupirira ndi madalitso a Mulungu kuti tipeza kusintha kwa uzimu m'dziklo lathu. Ndawerenga, ndipo zithandiza ntchito zanga zonse mwaosakhulupilira osiyanasiyana.

Mulungu akudalitseni,

Pastor R.B.

Lahore, Pakistan



Moni Wokondedwa M'busa Tony,


Bwana, pali Tony Alamo Christian Ministry imodzi yokha m'dziko, ndipo ntchito zake ndi zabwino. Kudzera m'mauthenga tikulandira anthu ambiri kwa Yesu. Bwana, ndikugawa zolemba zanu mu Punjab, ndipo mu mzinda anthu ambiri analandira zolemba zanu ndi mabuku. Pakufunka kwambiri mauthenga a Mulungu.

Bwana, ndikufuna kukwanirtsa Pakistan yense ndi nkhanu zanu zam'makalata za Tony Alamo, koteri ndikuthokoza Mulungu, tidzatsegula nthambi zatsopano ku Toba Tek Singh ndi Karachi, ndipo ndikuyembekeza kutsegula nthambi zambiri mu Pakistan. Chonde ndiyankheni posachedwapa. Zikomo, ndipo Mulungu akudalitseni.

Wanu mwa Khristu,

Pastor A.R.

Punjab, Pakistan



M'busa R.B. ndi mwana wake wamkazi kulandira maBaibulo, mabuku a Mesiya, ndi nkhanu za m'makalata kuti azigawa ku Lahore, Pakistan

## BABULO WA CHINSINSI MAKE WA ACHIGOLOLO

(Yachokera patsamba 2)

kulandira chipulumutso chanu pakunena pemphero ili:

AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.<sup>9</sup> Ndiukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.<sup>10</sup> Ndimakhulupiriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wamtengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhulukidwe.<sup>11</sup> Ndiukhulupiriranso kuti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WOYERA,<sup>12</sup> ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.<sup>13</sup> Ndiukutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe munitima mwanga, inu AMBUYE YESU.<sup>14</sup> Tsukani machimo anga ambirimbi achoke onse mu mwazi wamtengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.<sup>15</sup> Ndiukudziwa kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE YESU;

INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndiukudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.<sup>16</sup> MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyanse, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.<sup>17</sup> Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO mundiyankha komanso mundipulumutsa.<sup>18</sup> Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.<sup>19</sup>

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.<sup>20</sup> Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu*, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.<sup>21</sup>

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa M'busa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa ife kuti

mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kuperekwa chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipro anu] m'nhokwe zanga n'cholina choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mundiyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamatu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhalenso mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

9 Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 10 Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 11 Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 12 Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 13 Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 14 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 15 Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 16 Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14 17 Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 18 Aheb. 11:6 19 Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 20 Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 21 Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

*Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhanizina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembereni.*

**Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078**

**Lamyia ya pemphero ndi uthenga maola 24: +1 (661) 252-5686 • Fax +1 (661) 252-4362**

**www.alamoministries.com • info@alamoministries.com**

*Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imaperekwa zinthu zofunika Kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wavo wonse moyo wavo wonse ndi mphamvu zavo zonse*

**Mapemphero amachitika usiku uli wonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi Lamulungu nthawi ya 3 Koloko madzulo ndiponso 8 Koloko usiku ku Tchalitchi cha kudera la Los Angeles: 13136 Sierra Hwy., Santa Clarita, CA 91390, +1 (661) 251-9424**

**Magalimoto a ulere opita ndi kuchokera ku mapemphero amaperekedwa pa kona ya Hollywood Blvd. ndi Highland Ave., Hollywood, CA tsiku lili lonse nthawi ya 6:30 madzulo, Lamulungu lili lonse nthawi ya 1:30 madzulo ndi 6:30 usiku.**

**Mapemphero amachitika mu Mzinda wa New York Lachiwiri lili lonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi madera ena usiku okhaokha. Chonde imbani foni kuti mumve zambiri: +1 (908) 937-5723. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PA MAPETO PA MAPEMPHERO ALI WONSE**

*Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.*

*Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo*

*Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalamala yotumizira*

**Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalamala pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa +1(661) 252-5686.**

**M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).**

**MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.**

*Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:*